

NYA_TTB_1106_SCRIPT

1 Yohane : 4:5-9

Mutu : Akristu ayenera kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga.

Landirani moni wa Kumwamba inu wokonededwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye atitsogolera ndi mau apa Chibvumbulutso 4:19, amene akuti, “Onse amene ndiwakonda, ndiwadzudzula ndi kuwalanga; poterochita changu, nutembenuke mtima.”

Mupologalamu yatha, tinali kusanthula 1 Yohane 4:1-4, momwe timaunika nkhani yakuti wokhulupirira achenjere ndi aphunzitsi onyenga. Ndipo lero pa 1 Yohane 4:5-9, tipitiliza kuti akristu ayenera kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga.

5. Mwa ichi alankhula monga ochokera m'dziko lapansi, ndipo dziko lapansi liwamvera.

Pano Mtumwi Yohane akuonetsa chizindikiro chimodzi chimene iwo amene ali ndi Mzimu wokana Kristu angadziwike nacho. Iye akunena kuti anthu amenewa sali mumpingo wa Ambuye koma ali m'dziko. Awa, ndiwo aneneri ndi aphunzitsi onama, amene analowa m'dziko ndipo ali ndi Mzimu wotsutsa Kristu. Iwowa

analowa m'dziko ali wodetsedwa, ali ndi uchimo ndipo ali pansi paulamuliro wa tchimo. Uwu, ndiwo moyo wosasinthika, moyo wolamulidwa ndi thupi ndi m'dima, amene ayenda monga mwa mphamvu ya mulungu wawo (satana).Uyu, ndimulungu amene awatsogolera kuchita zonama ndipo amalamulidwa ndi thupi kotero kuti amafuna kuchita zinthu zadziko.Kutanthauza kuti pfundo, ziphunzitsa ndi zochita zawo zonse ndizofuna kukwaniritsa zochita za dziko, zomwe ndizosiyana kutali ndi zofuna za Kristu. Ichi, ndichimene Ambuye Yesu pa Yohane 17:14, adanena kuti, "Ine, ndawapatsaiwo mau anu; ndipo dziko lapansi lidana nawo, chifukwa sakhala a dziko lapansi, monga Ine sindikhala wa dziko lapansi." Komanso 1 Yohane 2:15, akunenetsa kuti, "Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, chikondi cha Atate sichiri mwa iye."

Ndiye pamene Yohane akuti, "Mwa ichi alankhula monga ochokera m'dziko lapansi," akunena kuti aphunzitsi onyengawa amalankhula zinthu zadziko lapansi komanso kuti iwowa akonda zinthu zadziko lapansi ndipoalibe chofuna ndi zolinga za Kumwamba. Mwanjira ina tikunena kuti sipobvutakusiyanitsa akristu ndi aphunzitsi

omwe ali ndi cholinga chopita Kumwamba ndi iwo amene amatumikiramzimuwadziko.

Tsono chinthu china chomwe tiyenera kuchidziwa ndichakuti, aphunzitsi onyengawa alindianthu ambiri owatsatira. Mwachimenechi, mukaonetsetsamupeza kuti magulu azipembedzo zonyenga, ndizomwe zikukula mofulumira kusiyana ndi chikristu. Ichi, ndichifukwa chakuti iwowa ali ndi mwawiwakuti amakwaniritsa zokhumba zathupi chomwe ife akristu sitichita. Tere tikunenetsa kuti ndichinthu chosathandiza kuti inu mupeze akristu chifukwa chofuna kukwaniritsa chosowa chathupi. Ndikunena mau amenewa chifukwa Ambuye Yesu mwini adanena pa Mateyu 6:33, kuti, “Koma muthangemwafuna Ufumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezozidzaonjezedwa kwa inu.” Tikunena kuti inu ndi ine, tiyenera kukhala tcherupanjira zomwe zikugwiritsidwa ntchito pofuna kukopa anthu kuti alowe mumpingo wa Mulungu. Kutanthauza kuti ngati inu mungagwiritse ntchito njira zathupi, Mulungu sadzawadalitsaonsewo. Apa, ndipamene tiyenera kuonetsetsa kuti mau a Mulungu akulalikidwa monga kuyenera.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kutsindika kunena kuti sizitanthauza kanthu kukhala ndi chimpingo chachikulu, koma chinthu chofunika ndi chakuti inu mupereke Uthenga wofunika. Kodi muutumiki kapena mumpingo wanu, mumaperekedwa mau a Mulungu? Kodi mau amenewa amaperekedwamwamphamvu ya Mzimu ndi kuti Mzimu wa Mulungu, ukhoza kutenga mauwo ndi kuwagwiritsa ntchito? Tsono tikunena kuti inu simuyenera kupereka Uthenga Wabwino mwanjira yokometsa, koma kupereka monga momwe uli. Mwanjira ina tikunena kuti, kodi mau a Mulungu amalalikidwa kuchokera ku mpingo wanu? Kapena tifunse kuti, kodi anthu akumdziwa Kristu kumpingo wanu?

Nkhani ikuti, inu pamene mufuna kuthandizira bungwe lina kuti litukuke, simusangalatsidwa ndi maonekedwe a nyumba zake, koma zotsatira za ntchito yomwe ikugwirika. Momwemonso Mulungu afuna inu ndi ine, kuti tisagwiritse ntchito nzeru ina yake yapadera pamene tikutumikira.

Tsono pamau akuti, “Alankhula monga ochokera m’dziko lapansi, ndipo dziko lapansi liwamvera,” tikuti pamene Yohane anagwiritsa

ntchito chitsanzo cha Kaini ndi abele, iye adanena kuti Kaini sanali wolungama ndipo sanali mwana wa Mulungu. Koma ndifuna muone kuti Mose sadanene kuti Kaini sanali wachipembedzo ayi. Taonani kuti Kaini anali kupereka nsembe kutsimikiza kuti anali m'chipembedzo. Tere ine, ndimakhulupirira kuti nsembe yake inali yokongola kwambiri mwina yoposa ya m'bale wake Abele. Tikunena kuti Kaini anapereka zipatso zokongola za m'munda mwake, pamene Abele anapereka nkhosa, mwina inali yosakondweretsa anthu ena. Koma nsembe ya Abele ndiyomwe Mulungu anailandira, popeza ndiyomwe inaonetsa uchimo wa munthu ndi kufunika kolandira Mpulumutsi. Pamene Kaini sanazindikire chimenechi, kutsimikizadi kuti zathupizimakhala kuthupi, ndipo sizigiwirizana ndi zauzimu. Ndiye muzinthu zonsezi tiyenera kuona kuti Yohane waonetsa bwino lomwe kwa ife kuti Yesu Kristu, ayenera kulalikidwa monga momwe Iye ali, osasintha konse. Ichi, ndichimene chidzachititsa kuti tione ngati chiphunzitsa chili choona kapena ayi.

6. Ife, ndife ochokera mwa Mulungu; iye amene azindikira Mulungu atimvera; iye wosachokera mwa Mulungu

satimveraife. Momwemo tizindikira Mzimu wa choonadi, ndi Mzimu wa chisokeretso.

Yohane mundime ino, akulankhula kwa iye mwini pamodzi ndi akristu anzake amene anaphunzitsa choonadi. Ndipo akutenga kuti chomwe iye akuphunzitsa ndichinthu chodziwika komanso choona pakati pa abale kotero kuti palibe wina angatsutse. Yohane akupereka umboni uwu, ndi cholinga chakuti akhazikitse chomwe iye akhulupirira ndi kuti pasaonekekumukaikira konse. Tere ndichifukwa chake pa Yohane 19:35, adanena mau akuti, “Ndipo iye amene anaona, wachita umboni, ndi umboni wake uli woona; ndipo Iyeyu adziwa kuti anena zoona, kuti inunsomukakhulupirire.”

Tsono cholinga cha umboni uwu, chinali chakuti akristu pamodzi ndi atumiki onse akhale m'moyo womwe usakhalewokaikitsa pakati pa anthu ena. Kutsimikiza kuti makhalidwe awo wolungama ndi woyera akhale wosakaikitsamkomwe. Tikunena kuti lero lino alipo akristu amakhalidwe abwino, wokhulupirika ndi wolungama. Ndiye pali chifukwa chanji, kuti akristu ena asakhale ndi khalidwe lomweli?

Ndiye pamau akuti, “Iye amene azindikira Mulungu atimvera...” Yohane akutanthauza kuti munthu aliyense amene akudziwa ndi kuonetsa khalidwe la Mulungu, ayenera kulandira chiphunzitso chake. Yohane anali kunena kuti popeza iye anali Mtumwi, yemwe anali munthu woyenera, kotero kuti anthu onse amene ndi woopa Mulungu amayenera kulandira Uthenga womwe iye anaphunzitsa. Ndiye taonani tsono Yohane akunena kuti, “Momwemo tizindikira Mzimu wa choonadi ndi Mzimu wa chisokeretso.” Mtumwi akunena kuti ife wokhulupirira tiri ndi kuthekera kuzindikira akristu amene analandira choonadi ndi iwo amene asanalandire choonadi. Kutsimikiza kuti ngakhale anthu achinyengowa atadzibisa motani, koma ngati alibe chiphunzitso choona chomwe chinaphunzitsidwa ndi atumiki oona a Mulungu, iwowa sayenera kutengedwa kuti ndi abwenzi kapena akristu oona ayi.

Wokondedwa anzanga apaulendo, inu ndi ine lero lino, tikhoza kugwiritsa ntchito muyeso omwewo pofuna kuzindikira atumiki oona kapena onyenga. Tikunena kuti ngakhale atumikiwa akhale achipembedzo motani, kaya khama ndi lutha, koma ngati

sangakhale ndi chidziwitso choona cha Kristu, sangabisale konse. Kutanthauza kuti chizindikiro chofunika kwambiri poonetsa kulungama kwa atumiki, ndiwo mtima wolandira zonse zomwe Mulungu amaphunzitsa. Ichi, ndichifukwa chake Ambuye Yesu pa Marko 10:15, akunenetsa kuti, “Ndithu ndinena ndi inu, munthu aliyense wosalandira Ufumu wa Mulungu ngati kamwana, sadzalowamo konse.” Tere, ndikunena ndichikhulupiriro chakuti ndiana a Mulungu okha amene angamve chiphunzitso choona ndipo sitiyembekeza kuti iwo amene asanatembenuke mtima kuti akhoza kulandira cha Mzimu ayi. Mwanjira ina utumiki wa Mulungu sungayembekeze chilimbikitso chochokera kwa anthu amenewa ayi.

Tsono tikunena kuti likasa la Mulungu limaimira Kristu, lomwe limanyamulidwapamapewaa ansembe. Momwemonso Kristu lero lino ayenera kunyamulidwapamapewandi kupita naye kudziko lonse lapansi. Ndiye chinthu chachikulu ndikuona ndichakuti Uthenga Wabwino udzalandiridwa ndi ana a Mulungu. Kunena kuti iwo amene anasankhidwa ndi Mulungu sadzanyengedwa nthawi zonse. Ichi ndichimene adanena Ambuye Yesu pa Yohane

18:37, kuti, “Yense wakukhala mwa choonadi amva mau anga.”Tere pamau amenewa ndifuna kunenetsa kuti pamene munthu akhala kutari ndi Ambuye Yesu, ndi atumiki a Kristu wokhulupirika, nakhazikika m’zinthu zadziko, iyeyu amalowerera kuchoka ku Mzimu wa Kristu. Uku, ndiko kusiyana pakati pa akristu oona ndi iwo amene ndi wonyenga. Ndiye tikunenetsa kuti chiphunzitso chimene chionetsa umunthu wa Mpulumutsi, ndichomwe chimatsogolera mkristu kuturuka kudziko ndi kulowa kwa Mulungu chitsimikizo cha Mzimu wachoonadiumasiyana ndi Mzimu wonyenga. Ichi, ndichimene Yohane afunitsitsa kuti inu ndi ine, tichidziwe bwino.

7. Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake: chifukwa kuti chikondi chichokerakwa Mulungu, ndipo yense amene akonda, abadwa kuchokera kwa Mulungu, namzindikira Mulungu.

Tiyeni pano tigwire mau akuti, “Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake.” Ndiye mwina mwafunsa kale kuti kodi pali chifukwa chanji kuti tikondane? Yankho likuti, inu ndi ine tiyenera kukondana wina ndi mnzake chifukwa Mulungu ndiye

chikondi. Payankhoili, ndifuna inu ndi ine, tisamalitse kwambiri pachimene Yohane akunena. Taonani iye wangotsiriza kumene kuchenjeza za aphunzitsi onyenga, amene sayenera kukondedwa ngakhale kupemphereredwa chifukwa anasankha kukhala ana a m'dierekezi. Ndiye sibwinokumawakhazikitsa mtima pansi kuti ndimakupemphererani ayi. Ife, tiyenera kupempherera ana a Mulungu ndi iwo amene asanamdziwe Kristu kuti alandire mau a Mulungu. Ndiye pamene Yohane wachoka kuchenjezo la aphunzitsi onyenga, tsopano watembenukira kuchiphunzitso cha gawo lina, chomwe chikuti wokhulupirira ayenera kukondana wina ndi mnzake.

Pano ndiyenera kukumbutsa kuti Yohane sakukamba za chikondi chomwe chimakhala pakati pa mwamuna ndi mkazi kapena pakati pa makolo ndi ana ayi, koma chikondi chapaderadera, chochokera Kumwamba. Ichi, ndichikondi chomwe Mzimu Woyera amalonga mkati mwathu ndipo ndi Mzimuwa Mulungu wokha womwe ungaonetsere chikondi chimenechi kwa ife. Kutsimikiza kuti ndichikondi cha Mulungu ndiponso kuti ndi Mzimuwa Mulungu wokha womwe ungapange ife kupereka chikondichi kwa anzathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna timvetsetse kuti ichi, sichikondi chomwe timangosangalatsidwa ndi anzathu ena ndi kumakhalanawo ayi. Mwanjira ina tikunena kuti anthu ambiri takhala tikugwiritsa ntchito chikondi ichi, molakwika. Tikunena kuti anthu ambiri tagwiritsa ntchito chikondi chokhala bwino ndi ena pakutembenuza kukhala chikondi pakati pa mwamuna ndi mkazi. Kunena kuti anthu ena akhala akumakhumudwa pamene agwiritsantchito chikondi ichi, pakufunsira mkazi kuti alowe naye paukwati. Mwachisoni kuti mkazi amanena kuti iye amangocheza nawo chabe, koma sawakonda kuti akhoza kukhala nawo paukwati ayi.

Nkhani ikuti pamene inu mukumana ndi munthu Wobadwa kwatsopano, amakukondanimwamtundu wina mwanjira yoonetsa kuti ndiye Wobadwa mwa Mulungu. Kutanthauza kuti amakukondani ndi chikondi chochokera Kumwamba popeza Mulungu ndiye chikondi, kasupewachikondi, muzu wachikondi, kholo ndi mtsogoleri wachikondi. Kutsimikiza kuti chikondi ichi, ndipopokolowekapo chilamulo chonse ndipo kuti cholinga chonse cha chilamulo ndi chikondi pa Mulungu ndi munthu mnzathu. Ichi,

ndichimene akunena Yohane pamene anati, “Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake: chifukwa chikondi chichokerakwa Mulungu.” Tikunena kuti chikondi ndilamulolochokerakwa Mulungu ndipo kuti ndilo lamulo lomwe limaonetsa chifuniro chake chomwe ndichomkondweretsa mwini. Chikondi ichi, chimachokera kwa Mulungu mwini chimene chiri mphatso ya chisomo chake ndi chipatso cha Mzimu wake chomwe chimaphunzitsaokhawo wotembenuka mtima wawo.

Apa, anali kunena kuti Mzimu wa Mulungu ndi Mzimu wa chikondi ndipo kuti moyo watsopano mwa ana a Mulungu ndicho chipatso cha chikondi. Paulo naye pa Agalatiya 5:22, anatsindika kunena kuti, “koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi...” Tikunena kuti munthu amene adziwa Mulungu kudzera mwa Kristu, amakonda iwo amene ali ndi chisomo cha Mulungu mkati mwawo ndi chithunzi cha Kristu pa iwo. Iyeyu ndiye adziwa mtima ndi chifuniro cha Mulungu chomwe chimaphunzitsidwa za kukonda abale. Kodi chipatso ichi, chimaoneka mwa inu?

8. Iye wosakondasazindikira Mulungu; chifukwa Mulungu ndiye chikondi.

Mtumwi Yohane akunenetsa kuti munthu amene sakonda ana a Mulungu, iwo amene anabadwa mwa Iye, sadziwa kukonda Mulungu, yemwe ali Atate wawo. Kutanthauza kuti munthu uyu, alibe malingaliro abwino a Mulungu, ndipo ngati alibe ulamuliro wachikondi mwa iye, sayenera kudziika kukhala wofanana ndi Kristu. Popeza Kristu ndiye chikondi, osati kuti analandira chikondicho ayi, koma Iye ndiye chikondicho. Kutsindika kunena kuti Mulungu sasintha ngakhale dziko lisinthe, kaya tikhale m'dziko la chisokonekero, chisawawa ndi la m'dima.

Tsono nkhani yonseyi ikulingapaganizo la Yohane lakuti mphunzitsi wonyenga ndiye munthu amene alibe chikondi ndipo kuti Mulungu ndiye chikondi. Ndiye popeza munthuyu alibe chikondi, zikutanthauza kuti sadziwa Mulungu, ndipo kuti munthuyu sadziwa chikondi. Kodi inu muli m'gulu liti, lodziwa chikondi kapena losadziwa chikondi? Koma njira imodzi yomwe inu mungaonetse kuti mumadziwa chikondi ndi yakuti inu mumakhudzidwa ndi moyo wa wokhulupirira mnzanu

9. Umochidaoneka chikondi cha Mulungu mwa ife, kuti Mulungu anamtuma Mwana wake Wobadwa yekha, alowe m'dziko lapansi kuti tikhale ndi moyo mwa Iye.

Pano tiyambensondifunso lakuti, kodi chikondi cha Mulungu chidaonekera motani? Yankho likuti, chikondi cha Mulungu chidaonekera pamtanda. Ndiye pa yankho ili, Mtumwi Yohane sakunena kuti palibe njira ina iliyonse momwe chikondi cha Mulungu chimaonekera ayi. Iye akuti, mwanjira zochuluka momwe chikondi cha Mulungu chingaonetsedwe, koma imfa ya Mwana wake, yemwe anachita kutumizidwa kuchokera m'Mwamba, ndiyo ikuonetsa poyera za chikondi cha Mulungu. Tamvani zomwe mtumwi akunena pa Yohane 3:16, pamene akuti, “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asataike, koma akhale nawo moyo wosatha.”

Tsono Yohane akunena kuti chikondi cha Mulungu chinaonetsedwa pamene Ambuye Yesu anafa ndi cholinga chakuti ife wokhulupirira tikhale ndi moyo wamuyaya. Tikunena kuti ndichizindikiro chachikulu cha chikondi cha Mulungu pa ife kuti anatumiza

Mwana wake Wobadwa yekha ndi cholinga chakuti ife mwa Iye, tikhale ndi moyo. Ichi, ndichifukwa chakuti Kristu ndiye moyo popeza anaombola moyo wathu umene unataidwa kudzera m'machimo athu. Tere chikondi chimenechi, ndichimene chiyenera kutikakamizaife kukonda wokhulupirira anzathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi mau akuti chikondi cha Mulungu ndi chodabwitsa popeza ifesitidamukonde, koma Iye ndiye adayambakutikonda. Kutanthauza kuti Mulungu anatikondaife ngakhale pamene ife tinalibe chikondi pa Iye, pamene ife tinali muuchimo, m'chisoni, momwe sitinali woyenera kulandira chikondi chimenechi, popeza tinali wodzala ndi machimo, wodetsedwa ndi uchimo kotero pamafunikadi wina amene angatitsuke ndi mwazi wake. Uyu, ndiye Kristu amene ali chikondi. Kodi inu mudalawa kale chikondi chimenechi?

Kwalerotilekeza pano. Ndipo timasanthula 1 Yohane 4:5-9, pamene timapitiliza kuona kuti akristu ayenera kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!